Baibulo ya bana
Yakubweleselani

# Zozizwisa za yesu



Yolembewa na: Edward Hughes

Yofotokozewa na: Byron Unger; Lazarus; Alastair Paterson

Yosinthiwa na: E. Frischbutter; Sarah S.

Yantanthauliziwa na: www.christian-translation.com

Yochosedwa na: Bible for Children www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chitupa: Muli na danga yojambula nakutulusa koma osagulisa.

Yesu anacita zozizwisa zambiri. Zimenezi zinali kusonyeza kyti yesu ndi mwana wa Mulungu. Cozizwisa choyamba chinacitika pa phwando ya ukwati.



Panapezeka bvuto lakuchepekela kwa vinyu kuti yense anali pa phwando pamenepo akwanile.



Dipo maria mai wake wa yesu anamuuza yesu za bvuto limeneli ndipo anauzanso ophunzira ake kuti achite cili conse comwe yesu azawauza.



Ndipo yesu anati kwa anchitowo “dzazani madzi m’mitsukoyi”.  Ndipo iwo anadzaza ndendende.



Ndipo iye anatinso kwa iwo “Tsopano tungani ndipo kaperekeni kwa mkulu wa pwando”. Ndipo madzi anasanduka vinyu, vinyu wabwino kamanso wopambana.



Ndipo antcihto anakondwela powona kuti yesu wasandusa madzi kukhala vinyu.



Ndimulungu cabe amene angathe kuchita zotelezi.



Yesu anachita cozizwisa china. Tsiku lina nthawi ya usiku anapita kunyumba ya petulo pamodzi ndi ophunzila ache, ndipo mpongozi wake wa petulo anali kudwala malungo.



Ndipo anawelama nadzudzula malungo ndipo anamusiya. Anadzuka nthawi yomweyo nayamba kuwatumikila.



Pamene dzuwa linkalowa anthu anabweresa kwa yesu onse amene anali ndi matenda osiyanasiyana ndi ziwanda kuti awathandize. Kodi yesu anatha?



Yesu mwana wa Mulungu anawathandiza. Onse amene anali odwala anawachirisa komanso olemala myendo anaima ndiku yenda komanso kuthamanga.



Wina anaza ndimatenda yakhate.



Anakhalanso bwino ndikuchirisidwa ndi yesu.



Azimai ndi azibambo onzunzidwa ndi ziwanda anaima pa maso pa yesu. Ndipo ziwanda zinatuka mwayiwo ndi mantha.



Amene analibe cimwemwe anasangalalanso.

Anyamata anai anayesa kuthandiza bwenzi lao amene anali wakufa ziwalo kupita naye kwa yesu, koma sakanakwanise chifukwa cha gulu lalikulu. Akanacita bwanji?



Anyamata aja ndichikhulupiliro cawo anasasula denga la chapamwamba pamene panali yesu...



…ndipo atabowoleza,
anatsisa mphasa pamene
wofa ziwaloyo
anagonapo. Tsopano
anali pafupi
ndi yesu.



Yesu ataona chikhurupiliro cawo, anati kwa wofa ziwalo “Mwana, machimo ako akhululukidwa”. Pamenepo anayima ali wolimba ndi mphamvu, yesu anamuchiritsa.



Pamene Yesu atalowa m'bwato ndi ophunzira ake, mwadzidzi mphepo yayikulu yamkuntho inawomba pa nyanjapo, kotero kuti bwato linayamba kumizidwa ndi mafunde.



Koma yesu anali mtulo. Ophunzira ake anapita namudzusa nati, “Ambuye tipulumuseni tikumira”.



Anadzuzula mphepoyo ndi mafynde ndipo nthawi imeneyo panali bata lalikulu panyanja. Ndipo ophunzirawo anadabwa nafunsa kuti “ndi munthu wotani uyu? Kuti ngakhale mphepo ndi mmafune zimvera iye”.



Ndipo ophunzira ake anakhulupilira kuti yesu analidi mwana wa Mulungu chifukwa zonse zimene anacita pakati pawo zinawonesa ulemelero wake. Ophunzira ake sanali kudziwa kuti azaona zambiri kwa yesu pamene anali kugwira nchito pakati pawo.



# Zozizwisa za yesu

Nkhani yofunila ku mau a mulungu, baibo

yupezeka mu

Mateyu 8-9, Mariko 1-2, Mariko 4, Luka 4, Luka 8, Yohane 2

"Kulowa kwa mau anu ni nyali."
masalimo 119:130

Kwatha

Nkhani zamu baibo zutiuzya zabwino pali mulungu anatipanga na zimene afuna.

Mulungu aziba tachita zoipa zambili, yamene amaita machismo. Mphoto ya chimo ni ifya, koma mulungu atikonda kwambili kuti etuma mwana wake okondeka yesu, kuti azatifela pa mtanda nakunzuznzika pamachimo anu. Yesu anabwelela ku umoyo ndipo naenda kumwamba. Ngati mukhulupilila mwa yesu nakumupempha kukukhulululkila mchimo. Azachita. Azabwela kunkhala mwa iwe ndipo uzankhala muyayaya.

Ngati ukhulupilila mu zoona, Kamba izi kwa mulungu: yesu, nikhulupilila kuti ndiwe mulungu ndipo ndiwe muthu ananifela pamachimo anga.  Bwela muumoyo wanga nakukhuluka machismo anga kuti nikhale na umoyo wasopano ndipo siku lina nikakhle naiwe pamozi muyayaya. Nithandizeni kukulemekezani nachnkhala mwana wako.  Ameni.

Welengani baibo nakukamba na mulungu nsiku zones.   Yohane 3:16